


**Maphunziro a chidule a Baibulo kwa a Khristu a tsopano komanso amene akukula kumene**

Copyright © 2022

Charles "Chic" Shaver, *Mlembi*

**MALONJE KWA OPHUNZIRA**

Tsopano ndinu Mkhristu. Mukufunika kuphunzira kukula ngati Mkhristu. Muphunzira maphunziro asanu ndi atatu a kukula ngati Mkhristu.

Phunzirani phunziro liliilonse pa nokha. Werengani Baibulo. Yankhani mafunso m'mene mungathere. Kenako, kumanani ndi m'phunzitsi kapena m'busa wanu. Adzayankha mafunso amene simukuwadziwa. Akakuthandizani kumvetsa maphunziro.

Mudzapeza vesi la Baibulo loloweza mu phunziro lililonse. Lowezani. Mavesi akuthandizani kukula Mkhristu.

Nthawi zina, mudzaona mawu olembedwa akuda kwambiri, **ngati apa.** Awa ndi mawu kapena ziganizo zifupizifupi zimene zikhoza kukhala za chilendo. Pamapeto pa phunziro lililonse, mudzapeza mndandanda wa mawu okhala ndi kufotokozera kwake mwa chidule.

Mulungu amakukondani kwambiri.  Akufuna akhale Mulungu wanu. Akufuna inu muphunzire za iye. Mukhoza kuyankhula ndi Mulungu. Mukhoza kumupempha kuti akuthandinzeni. Adzakuthandizani kumvetsetsa. Adzakuthandizani kuphunzira.

**MALONJE KWA M'PHUNZITSI**

Perekani buku ili kwa Mkhristu wa tsopano pa nthawi ya kutembenuka mtima kwake, kapena akangotembenuka kumene. Limbikitsani munthuyo kuwerenga maphunziro ndi kuyankha mafunso m'mene angathere. Funsani munthuyo kuchita phunziro limodzi lokha pa nthawi. Yesetsani kukhazikitsa nthawi sabata iliyonse kukumana ndi ophunzira kuti mukambirane phunziro.

Ngati ophunzira sangawerenge phunziro pa wokha, khazikitsani nthawi imene mungawerenge ndi kukambirana maphunziro pamodzi. Pamene ziri zofunikira kuchita phunziro limodzi pa nthawi, zikhoza kukhala zofunikira kukhala ndi zigawo zophunzira zoposera kamodzi ndi phunziro lililonse. Thandizani ophunzira pa kuyang'ana malemba mu Baibulo. Yankhani mafunso pamodzi, kuwonetsetsa kuti ophunzira wamvetsetsa phunziro musanapite pa phunziro lina. (Mayankho olondola akhoza kupezeka mu Mawu owonjenzera.)

**Phunziro 1**
**A KHRISTU NDI A MULUNGU**

***Vesi Loloweza:***

> Yesu anati, "Taonani ndayima pakhomo ndi kugogoda. Ngati wina amva mawu anga natsekula chitseko, ine ndidzalowamo" (Chivumbulutso 3:20).

Pa funso lililonse m'musimu, pezani ma vesi a maphunziro a Baibulo kapena Chipangano cha Tsopano. "Yohane 1:12" amatanthaunza buku la Yohane, chaputala 1, vesi 12. Pezani mndandanda wa ma buku koyambilira kwa Baibulo. Mupeza ma nambala a ma peji a mabuku onse. Pitani pa nambala ya peji pamene mabuku amayambira. Pezani mavesi a Baibulo ndipo werengani. Werengani chiganinzo komanso funso lililonse mu maphunziro. Lembani mayankho m'mawu anu anu. Kapena, gwiritsani ntchito mawu ochokera mu Baibulo. (Mavesi ochokera mu Chipangano Chakale alembedwa kwa inu.)

1. Werengani Yohane 1:12. Ndalandira Yesu **mu mtima mwanga.** Ndikukhulupirira Yesu Khristu ndi Mulungu. Yesu ndi **Mpulumutsi** wanga. Ndine **Mkhristu.** Kodi izi zikutanthauza kuti ndine mwana wa Mulungu? (inde kapena ayi)

2. Yesu ndi bwenzi la anthu onse amene amamulandira iye. Yesu akufuna kulowa **m'mitima yathu.** Akudikira kuti abwere. Koma, tikufunika kumupempha kuti abwere. Werengani Chivumbulutso 3:20 ndipo yankhani mafunso otsatirawa.

    a) Kodi ndi ndani amene akufuna kulowa **m'mitima yathu?**

    b) Kodi ndi ndani amene angayankhe mawu a Yesu?

    c) Kodi Yesu akufuna kuti ine ndichite chiyani?

    d) Kodi Yesu Khristu adzachita chiyani ngati nditatsegula khomo la mtima wanga?

    e) Kodi mwamufunsa Yesu kulowa **mu mtima mwanu?** (inde kapena ayi)

f) Kodi ndinu **mkhristu** tsopano? (inde kapena ayi)

3. Werengani Luka 19:20. Kodi Yesu anabwera kudzapulumutsa anthu amene ali otaika? (inde kapena ayi)

| |
|---|
| Otaika amatanthauza aliyense amene sadziwa Yesu ngati mpulumutsi. |

4. Werengani Aroma 3:23.

a) Kodi ndi chifukwa chiyani anthu ali **otaika?**

b) Kodi ndi chifukwa chakuti anachimwa? (inde kapena ayi)

c) Kodi Aroma 6:23 amatanthauza chiyani akati **chimo** "limalipira" kapena kubweretsa imfa?

d) Kodi izi zikutanthauza kuti **chimo** limalekanitsa **ochimwa** kwa Mulungu? (inde kapena ayi)

| |
|---|
| **Ochimwa** adzakhala ku **ganena** akadzamwalira. Koma, Yesu Khristu amapereka kwa **okhulupirira** mphoto ya **moyo wosatha. Okhulupirira** adzakhala **kumwamba** akadzamwalira. |

5. Werengani Aroma 5:8. Kodi ndi ndani amene anatifera pamene tinari ochimwa?

6. Pezani buku la 1 Yohane. Lili kufupi ndi kumapeto kwa Chipangano Chatsopano. 1 Yonane ndi limodzi mwa ma buku a Yohane. Werengani 1 Yohane 1:9. Kodi Mulungu adzachita chiyani ngati tivomereza **machimo** athu?

| |
|---|
| **Kuvomereza** kumatanthauza kuvomera kwa **Mulungu kuti ndife ochimwa.** |

7. Yesaya 55: 7 amati: "Woyipa asiye makhalidwe ake oyipa, ndipo osalungama maganizo ake" amatinso: "abwerere kwa Yehova, ndipo **adzawakhululukira." Alape machimo** awo. Yankhani mafunso otsatirawa

a) Kodi woyipa asiye kuchita chiyani?

b) Kodi achite chiyani ndi maganizo awo woyipa?

c) Kodi Mulungu adzachita chiyani akalapa?

8. Pezani Aefeso 2: 8- 9. Kodi yankho lolondola ndi liti? (a, b, kapena c) Kodi ndi njira iti yakuti ine kapena wina aliyense **apulumutsidwe?**

a. Ndiyenera kugwira ntchito yambiri.

b. Ndiyenera kuyesetsa **kudzipulumutsa ndekha.**

c. Ndiyenera kukhulupirira Yesu Khristu kuti **andipulumutse.**

9. Werengani Aefeso 2:10.

a) Kodi tiyenera kuchita chiyani **tikapulumutsidwa?**

b) Kodi ntchito zabwino zimatipulumutsa?

10. Kodi ndi ndani amene timamudziwa kudzera mwa Yesu Khristu. (Yohane 14:6 ndi 14:9)

11. Werengani 1 Yohane 5:13. Kodi **okhulupirira** angadziwe kuti tsopano ali ndi **moyo wosatha?** (inde kapena ayi)

12. Werengani Yonane 6:47

a. Kodi munthu amene amakhulupirira Yesu ali ndi **moyo wosatha?** (inde kapena ayi)

b. Kodi izi zikutanthauza kuti ndidzakhala mpaka muyaya? (inde kapena ayi)

c. Kodi ndidzakhala kuti ndikadzafa?

13. Kodi mukudziwa kuti ndinu mwana wa Mulungu? Ngati ndi zoona, kodi mungafotokoze m'mene mukudziwira m'mawu anu anu?

| |
|---|
| Yesu wapereka moyo watsopano kwa inu. Tsopano, kodi mukhoza kukula motani ngati mkhristu? Apa pali njira zina zofunikira kuti mukule. |

*Werengani Baibulo tsiku ndi tsiku.* Werengani Mateyu 4:4. Tsopano, werengani chaputala mu buku la Yohane tsiku ndi tsiku. Maphunziro awa ali ndi mafunso ochokera mu buku la Yohane komanso kuchokera m'ma buku ena mu Baibulo. Werengani vesi loloweza la phunziro lililonse. Lowezani lililonse.

*Pempherani tsiku ndi tsiku.* Yankhalani ndi Mulungu. palibe mawu a paderadera amene muyenera kunena. Yankhulani kwa Mulungu ngati m'mene mumayankhulira ndi bwenzi lanu la pamtima.

*Pitani ku tchalichitchi m'mene mungathere.* Pitani ku mpingo umene umalalikira zochokera mu Baibulo. Pitani ku mpingo umene umalalikira za Yesu. Muyenera kukhala ndi **a Khristu** ena. Adzakuthandizani kukhala mwa Yesu.

*Mmverani Mulungu.* Mufunseni Ambuye akuthandizeni. Adzakuuzani zoyenera kuchita. Adzayankhula kwa inu kudzera mu Baibulo. Adzayankhula kwa inu mu tchalitchi. Pamene mukudabwa kuti muchite chiyani, dzifunseni, "Kodi Yesu akanachita chiyani?" Yankho lidzakuthandizani kumvera Mulungu.

*Chitirani umboni kwa anthu ena.* Uzani wina wake zimene Yesu anakuchitirani. **Chitirani umboni** kwa anthu ena kuti tsopano ndinu **mkhristu.**

Tsopano, muyenera kuvetsetsa bwino kuti **Mkhristu** ndi ndani. Ichi ndi chiyambi chabe cha moyo wanu wa **chi Khristu.** Pali chimwemwe chambiri chimene chikubwera!

*MNDANDANDA WA MAWU*

1. **okhulupirira** *(dzina):* Anthu amene amakhulupirira mwa Yesu Khristu ngati **mpulumutsi** wawo; anthu amene amalandira Yesu **m'mitima mwawo;** anthu onse amene ali a Khristu.

2. **Mkhristu** (*dzina la mwini mwini):* Munthu amene **amalapa machimo** ndipo amakhulupirira mwa Yesu; munthu amene amatsatira ndi kumvera YesuKhristu.

3. **kuvomereza** (*mneni*) Muuzeni Mulungu kuti mukudziwa kuti ndinu **wochimwa;** muuzeni Mulungu za **machimo** anu komanso maganizo komanso ntchito zoipa.

4. **Moyo wosatha** (*dzina la mawu)*; Moyo umene Mulungu amapereka; moyo ndi Mulungu tsopano lino komanso ndi Iye mpaka muyaya **kumwamba.**

5. **khululukira** (*mneni)*: kusapereka chilango kwa wina wake chifukwa cha maganizo ndi ntchito zawo zoipa; (Mulungu **amakhululukira** ndi kuiwala **machimo** athu **tikalapa.)**

6. **kumwamba** (*dzina)*: kwawo kwa **a Khristu** akamwalira.

7. **Gahena** (*dzina)*: malo amene **wochimwa** amalangidwa akamwalira.

8. **mu mtima mwanga; m'mitima yathu** (*liwu la mbuyo la mawu osaima pawokha*): mkatikati mwa munthu; mkatikati mwa anthu;(Mtima umakhala ndi maganizo, chisankho komanso zofuna za anthu.)

9. **wotaika** (*mfotokozi)*: kusapeza njira kwa Mulungu; popanda chiyembekenzo cha **moyo wosatha;** kusadziwa Yesu ngati **mpulumutsi.**

10. **lapani** (*mneni)*:  kufunsa Mulungu kuti **akhululuke machimo;** kuchoka ku **uchimo** kupita kwa Mulungu.

11. **pulumutsa; amapulumutsa** *(mneni)* kumasula kuchoka ku uchimo (Yesu Khristu **amapulumutsa** kapena kutisambitsa **machimo athu.** Choncho. **Amatipulumutsa** kuti tisalangike ku **gahena.)**

12. **Mpulumutsi** (*dzina la mwinimwini):* Yesu Khristu; amene **amatipumutsa** kuchoka ku **machimo**.

13. **chimwa** (*mneni):*  **machimo** (*dzina)*: kuchita ntchito zoipa ndi kuganiza maganizo woyipa; kusavera Mulungu; maganizo kapena ntchito zoipa.

14. **wochimwa** (*dzina)*: Munthu amene satsatira malamulo a Mulungu; munthu amene **amachimwa.**

15. **chitira umboni** (*mneni)*: kuuza ena za Yesu Khritsu; kunena zimene Yesu wakuchitirani.

**Phunziro 2**
**AKHRISTU AMAYENDA NDI MULUNGU**

***Vesi Loloweza:***

> "Sichinakugwereni inu chiyeso koma cha umunthu, koma Mulungu ali okhulupirika amene sadzalora inu kuyesedwa koposa kumene mukhoza, koma pamodzi ndi chiyeso adzaikanso populumukira kuti mudzakhoza kupilirako." (1 Akorinto 10:13).

Akhristu a tsopano ali ngati makanda mwa njira ina yake. Ana amakula akabadwa. A Khristu ayenera kukula ngati okhulupirira a tsopano mwa Yesu. A khristu amakula akamavera Mulungu. kukula kwathu timakutcha "kuyenda ndi Mulungu." Mika anati, "kuyenda ndi Mulungu wako modzichepetsa" (Mika 6:8). Mika anali mneneri mu Chipangano Chakale.

Pezani ndi kuwerenga mavesi a Baibulo awa. Ndipo yankhani mafunso otsatirawa ndi mawu anu anu. Kapena gwiritsani ntchito mawu kuchokera mu mavesi a Baibulo.

1. Buku la Yona limatiuza m'mene tingayendere ndi Mulungu.

    a. Werengani Yohane 8:12. Kodi a Khristu amakhala kkapena kuyenda mu mdima? (Inde kapena ayi)

    b. Kodi Mulungu amafuna kuti tiziyenda mkuwala kumene kumatipatsa moyo? (inde kapena ayi)

    c. Werengani Yohane 1:37. Kodi ndi ndani amene a Khristu ayenera kumutsatira?

    d. Werengani Yohane 2:5. Kodi a Khristu achite zonse zimene Yesu amawauza kuti achite? (inde kapena ayi)

    e. Werengani Yohane 5:14. Kodi a Khristu asiye kusamvera Mulungu?

2. Werengani 1 Petro 5:8. Kodi ndi ndani amene amene safuna kuti ife tiziyenda ndi Mulungu?

3. Werengani Mateyu 4:1. Kodi **Satana** anachita chiyani kwa Yesu Khristu?

4. Werengani Ahebri 4 :14 -15. Baibulo limati Yesu **anayesedwa.** Kodi Yesu **anagonjera** ku **yesero?** (inde kapena ayi)

| |
|---|
| **Yesero** ndi chimo si zofanana. **Yesero** ndi kutsogozedwa kapena kuitanidwa kuchita choipa. Kodi **yesero** chimo? (inde kapena ayi) |

5. Tipemphere kwa Mulungu **Satana akatiyesa.** Timalimbana ndi **Satana** ndi thandinzo la Mulungu. Werengani Yakobo 4:7. Kodi tichite chiyani satana **akamakuyesani?**

6. Werengani Yakobo 4:17 ndi 1 Yoyane 3:4. Kodi chimo ndi chiyani?

7. Yesaya 59:2 amati, "Koma zoipa zanu zakulekanitsani inu ndi Mulungu wanu." Kodi chimo langa limandisiyanitsa ndi Mulungu? (inde kapena ayi)

8. Werengani 1 Yohane 3:9.

   a. Kodi vesi la Baibulo ili likutanthauza chiyani kwa inu?

   b. Kodi mwana wa Mulungu amapitiriza kuchimwa?

9. Werengani 1 Akorinto 10:13. Kodi lonjezo la Mulungu kwa ife ndi chiyani? (a kapena b)

   a. Mulungu adzandithandiza kuthawa **yesero.** Adzandithandiza kuti **ndisagonjere** ku **yesero**

   b. Mulungu sadzandithandiza kuthawa **yesero.** Sadzandithandiza pamene **ndikuyesedwa**

10. 1 Yohane 2:1 amati Yohane analemba buku ili. Kodi ndi chifukwa chiyani Yohane analemba buku ili?

11. Werenganinso 1 Yonane 2:1. A Khristu asamachimwe. Kodi yankho la bwino ku funso ili ndi liti? (a, b, c, kapena d)

   a. anene kuti sangathandinzire kuchimwa. Anene kuti Satana anawapangitsa kuti achimwe.

b. akhale ngati sanachimwe mkomwe.

c. avomereze machimo kwa Yesu ndi kulapa. Ndipo apitilire kukhala ndi Mulungu.

d. asiye kukhala moyo wa chi Khristu. Aziva kuti sangakhale ndi Yesu.

12. Werengani 1 Yohane 1:9. Mulungu safuna kuti tizichimwa. Koma, kodi adzatikhululukira ngati titachimwa? (inde kapena ayi)

| |
|---|
| Amatikhululukira tikavomereza machimo athu ndi kulapa. |

13. Werengani Yohane 14 :21. Kodi timawonetsa chiyani tikamumvera?

14. Werengani Yohane 10:27 -28. "Nkhosa" mu vesi ili zikutanthauza a Khristu. Kodi amene ali ndi moyo wosatha ndani?

| |
|---|
| Yesu ndi m'busa wabwino amene amasamalira nkhosa. Yesu amadziwa aliyense amene ali Mkhristu. Kodi ndi zofunikira kwa Mkhristu kutsatira Yesu Khristu? (inde kapena ayi) |

Tsopano yendani ndi Mulungu. **Osagonjera** ku **yesero.** Mverani Mulungu. Tsatani Yesu tsiku ndi tsiku

*MNDANDANDA WA MAWU*

1. **mdierekezi** (*dzina*): mzinu Woyipa umene **umayesa** anthu kuti achite zoipa; mzimu woipa wamphamvu kwambiri; (**mdierekezi** amalimbana ndi Mulungu.)

2. **Mneneri** *(dzina):* munthu amene amayankhulira Mulungu; (**Mneneri** amapereka uthenga kwa anthu ochokera kwa Mulungu.)

3. **Imani** (*mneni*): kusagonjera **ku yesero; (kuima** pa vesi kutanthauza kukhala wa mphamvu mwa Ambuye. **Kuima** kumatanthauza kusachimwira Mulungu.)

4. **kuyesa, kuyesedwa** (*mneni)*: kuyesa kupanga munthu kuti achimwe kapena kuchita choipa.

5. **yesero, mayesero** *(dzina)*: chilichonse chimene chimaitana kapepa kutsogolera munthu kuti achimwe; kapena kuchita choipa; mchitidwe **oyesedwa** ndi **mdierekezi; mdierekezi** kupangitsa kuti munthu achimwe.

6. **dalira** (*mneni)*: kukhulupirira Mulungu kwa thunthu; kukhala ndi chikhulupiriro mwa; kukhulupirira mwa thunthu.

7. **gonjera** (*mneni*): kugonjera; kunena kuti "inde" ku chimo; kuchita zimene sitiyenera kuchita.

**Phunziro 3**

## AKHRISTU AMAPHUNZIRA KUCHOKERA KWA MULUNGU

***Vesi Loloweza:***

> "**Ndasunga mawu anu mu mtima mwanga** kuti ndisakuchimwireni" (Masalmo 119:11).

Baibulo ndi **Mawu a Mulungu**. limatiuza za chikonzero cha Mulungu cha miyoyo yathu. Limatiuza za chikonzero cha Mulungu cha dziko la pansi. Werengani Baibulo tsiku ndi tsiku kuti mupeze choonadi cha Mulungu. werengani Baibulo kuti mudziwe malonjezano ake pa ife.

Yankhani izi m'mawu anu anu. Kapena, gwiritsani ntchito mawu a mavesi a mu Baibulo.

1. Werengani Yohane 17:17. Kodi **Mawu a Mulungu** ndi choonadi?

| |
|---|
| **Mawu a Mulungu** ndi chiphunzitso chake kwa ife. |

2. Werengani 2 Timoteo 3:16. Kodi timadziwa motani kuti **Malemba** ndi choonadi cha Mulungu?

| |
|---|
| **Malemba** onse **anawalembetsa ndi Mulungu** kapena kuwuzira. Izi zikutanthauza kuti anachokera kwa Mulungu. Mulungu anatsogolera maganizo kwa anthu amene analemba Baibulo. |

3. Nenani zimene **Mawu a Mulungu** kapena **Malemba** adzachita kwa ife mu mavesi otsatirawa.

   a. Werengani 2 Timoteo 3:15. Kodi **Mawu a Mulungu** adzatipanga kukhala a nzeru ku chipulumutso? (inde kapena ayi)

   b. Werengani Yohane 15:3. Kodi **Mawu a Mulungu** adzatiyeretsa m'mitima mwathu? (inde kapena ayi)

   c. Werengani machitidwe 20 :32. Kodi **Mawu a Mulungu** azatipatsa mphamvu? (inde kapena ayi)

4. **Mawu a Mulungu** ndi ofunikira kwa a Khristu. Pezani Yohane chaputala cha 8. Mavesi ambiri amanena zimene tiyenera kuchita ndi **Mawu a Mulungu.**

   a. Werengani Yohane 8:54-55. Yesu anadziwa Mulungu, Atate. Kodi Yesu anachita chiyani ndi mawu a Mulungu?

   b. Werengani Yohane 8: 37. Anthu ena salandira chiphunzitso cha Yesu. Alibe malo a mawu Ake. Kodi izi zikutanthauza kuti sasunga **Mawu a Mulungu?** (inde kapena ayi)

   c. Werengani Yohane 8:47. Okhulupirira ndi wake wa Mulungu osati kwa mdierekezi. Kodi okhulupirira amachita chiyani za **Mawu a Mulungu?**

   d. Kodi okhulupirira amamva zimene Mulungu amanena? (inde kapena ayi)

   e. Werengani Yohane 8:31. Kodi **ophunzira** adzachita chiyani ndi **Mau a Mulungu?**

   f. Kodi ophunzira adzavera **mawu a Mulungu?**

   g. Werengani Yohane 8:51. Kodi tingakhale ndi moyo wosatha motani?

   h. Kodi ndi zoyenera kumvera **mawu a Mulungu?** (inde kapena ayi) (inde kapena ayi)

| |
|---|
| Yesu anati anavera Mulungu, Atate wake. Yesu anasunga **Mawu a Mulungu.**<br>Tiyeneranso kumvera Mulungu, Atate wathu, |

5. Werengani Yohane 14:23. Kodi ndimamuwonetsa chiyani Yesu pamene nditsatira ziphunzitso zake?

6. Werengani Yohane 20:31.

   a. Kodi **Mawu a Mulungu olembedwa** amatiuza za Yesu, mwana wa Mulungu? (inde kapena ayi)

b. Kodi Yesu Khristu amapereka chiyani kwa okhulupirira?

7. Werengani Aefeso 6:17. Mdierekezi amayesa kutigonjetsa m'miyoyo yathu ya chi Khristu. Amatiyesa ndikuyesetsa kutipangitsa kuti tichimwe.

a. Kodi tingagwiritse ntchito chiyani kuti tigonjetse mdierekezi?

b. Kodi lupanga la Mzimu ndi chiyani?

8. Werengani Mateyu 4:4, 4:7; komanso 4:10

a. Kodi Yesu anamuyankha motani mdierekezi?

b. Kodi ndi chifukwa chiyani Yesu anagwiritsa ntchito mavesi a malemba?

9. Werengani Masalmo 119:10-11.

a. Kodi Baibulo lidzakuthandizani motani kuti musachimwe?

b. Kodi ndi chifukwa tiyenera kutenga **Mawu a Mulungu** mu mtima?

10. Kodi ndi choona chotani **M'malemba** chimene chakuthandizani?

11. Baibulo limakuthandizani kukula ngati Mkhristu? (inde kapena ayi)

| Ngati yankho lanu ndi "inde," fotokozerani m'mawu anuanu kuti choonadi ichi ndi chiti? |
|---|

12. **Ophunzira** a Yesu ayenera kuphunzira ndi kuwerenga Baibulo tsiku ndi tsiku. Kodi munganene kuti ndi chifukwa chiyani m'mawu anu anu?

Taphunzira m'mene Mkhristu amaphunzilira kuchokera kwa Mulungu. taphunzira kuti ndi chifukwa chiyani Baibulo ndi lofunikira kwa **ophunzira.** Mu phunziro lotsatira, tiphunzira njira ina imene a Khristu amakulira.

*MNDANDANDA WA MAWU*

1. **ophunzira** (*dzina)*: okhulupirira; munthu amane amatsata Yesu Khristu; munthu amene akufuna kuphunzira zambiri za Yesu; munthu amene akufuna kuphunzira **Mawu a Mulungu.**

2. **anawalembetsa ndi Mulungu** *(mfotokozi)*: anachokera kwa Mulungu.

3. **Mawu a Mulungu:** (onani **Mawu a Mulungu.)**

4. **owuziridwa** *(mfotokozi)*: anachokera kwa Mulungu; anapereka nzeru kwa; (Mulungu; **anauzira** anthu woyera mtima kuti alembe mawu ake.)

5. **Malemba** (*dzina la mwini mwini*): Baibulo; mawu a Mulungu; (Mulungu anathandiza anthu Woyera mtima kulemba Baibulo.)

6. **kusunga mawu anu mu mtima** (*mneni wa liwu losaima palokha*): kukhulupirira ndi kumvera mawu a Mulungu; kuphunzira ndi kumvetsa zimene Mulungu ananena mu Baibulo.

7. **Mawu a Mulungu;** (*liwu la la m'mbuyo la dzina la mwini mmwini*): Baibulo Loyera, Malemba; choonadi cha Mulungu; zimene Mulungu amanena kwa anthu

**Phunziro 4**

## AKHRISTU AMAYANKHULA NDI MULUNGU

***Vesi Loloweza:***

> Yesu anati, "Kufikira tsopano simunapempha kanthu m'dzina langa; pemphani ndipo mudzalandira" (Yohane 16:24)

A Khristu amafunika aziyankhula ndi Mulungu. Ndi wa mphamvu kuposa wina aliyense kumwamba ndi pa dziko. Tiyenera kuyankhala naye tsiku ndi tsiku. Anthu ambiri amapeza kuti nthawi ya mmamawa kukhala nthawi yabwino. Tiyenera kuyankhala naye mu nthawi ya bata. Davide, analemba Masalmo ambiri akuti: "M'mawa, Yehova, mudzamva mau anga; m'mawa, ndidzakukonzerani pemphero langa, ndipo ndidzadikira." (Masalmo 5:3)

Kodi china ndi chiyani chimene Baibulo limatiuza za pemphero? Tiphunzira yankho mu phunziro iri. Yankhani mafuns awa mu mawu anu anu. Kapena gwiritsani ntchito mawu ochokera mu mavesi a Baibulo.

1. Werengani Marko 1:35. Kodi Yesu anapemphera nthawi yanji?

2. Werengani Luka 18:1. Kodi ndi ma ulendo ochuluka motani amene Yesu ananena kuti tiyenera kupemphera?

3. Werengani 1 Atesalonika 5:17-18. Kodi tiyenera kuchita chiyani pamene tipemphera?

| Tiyamika Mulungu chifukwa cha chimene anachita mwa Yesu Khristu. |
|---|

4. "Ndikadesekera zopanda pache mu mtima mwanga, Ambuye sakanandimvera" (Masalmo 66:18)

    a. Kodi ndi chifukwa chiyani pemphero siliyankhidwa?

    b. Kodi ndiyenera kusunga chimo mu mtima mwanga? (inde kapena ayi)

5. Werengani 1 Yohane 5:14.

a. Kodi vesi ili likutiuza m'mene tiyenera kupemphelera? (inde kapena ayi)

b. Kodi tiyenera kupemphera motani?

| |
|---|
| Tiyenera kupempha zinthu zimene ziri mu **chifuniro cha Mulungu**. |

6. Timaphunzira za pemphero mu buku la Yohane.

a. Werengani vesi loloweza Yohane 16:24. Kodi ndi **mwayi** wanji wa Akhristu?

b. Kodi ndi zotheka a Khristu kupempha china chilichose m'dzina la Yesu? (inde kapena ayi)

| |
|---|
| Komabe, a Khristu nthawi zonse ayenera kukpemphera **chifuniro cha Mulungu** kuti chichitike. |

c. Werengani Yohane 14:13. Yesu amayankha mapemphero athu. Kodi izi zimabweretsa **ulemero** kwa ndani?

| |
|---|
| Timapereka **ulemero** kwa Mulungu Atate chifukwa cha zimene wachita. |

d. Werengani Yohane 15:7. Kodi tiyenera kuchita chiyani kuti Yesu ayankhe mapemphero athu?

| |
|---|
| Tiyenera kuyesetsa kukhala mwa Yesu nthawi zonse. Mulungu adzatithandiza kuti tikhale mwa Iye. |

7. Werengani Mateyu 21:22. Kodi ndiyenera kuchita chiyani kuti ndilandire yankho la pemphero?

| |
|---|
| Izi zitanthauza kuti ndiyenera kudalira Mulungu. Ndiyenera kukhala ndi chikhulupiro kuti ayankha mapemphero anga. |

8. Werengani mavesi awa ndi kuganizira za zinthu zimene mukhoza kupemphelera.

- Mateyu 6:11
- Mateyu 9:38
- Afilipi 1:9
- 1 Timoteo 2:2
- Yakobo 1:5

9. Werengani Mateyu 26:41. Kodi ndiyenera kuchita chiyani pamene ndayesedwa kuti ndichimwe?

| |
|---|
| Mulungu adzatithandiza kuti tisachimwe. Tikhoza kumufunsa kuti atithandinze. |

10. Kodi Yesu amafuna kuti tizipemphera motani? (a, b, kapena c) Yesu amafuna kuti:

    a. Tizigwiritsa ntchito mawu a chipembedzo.

    b. Tizinena mawu okhawo a m' Baibulo.

    c. Tizimuuza zimene ziri mmitima yathu.

11. Kodi muli ndi ndondomeko ya nthawi yanu ya mapemphero? (inde kapena ayi)

12. Kodi mungachite chiyani za kuyankhula ndi Mulungu? fotokozerani mu chiganinzo chimodzi pa chikonzero chanu cha pemphero.

| |
|---|
| Pemphero ndi **mwayi!** Mukhoza kuyankhula ndi Mulungu. Ali ndi mphamvu ya kuyankha mapemphero anu. Mulungu amakukondani kwambiri. **Amakudalitsani** tsiku ndi tsiku. Amakudlitsani ndi zinthu zambiri. **Amakudalitsani** mu njira zambiri. |

Tsopano, mukhoza kuchitira china chake Mulungu. phunzirani phunziro lotsatira kuti muphunzire zimene mungachite.

*MNDANDANDA WA MAWU*

1. **amadalitsa** (*mneni*): amapereka zinthu zabwino kwa; amathandiza mwa njira ya paderadera; amapangitsa chimwemwe.

2. **ulemelero** (*dzina*): matamando, ulemu, ndi kulambira.

3. **mwayi,** (*dzina*) m'chitidwe wa paderadera kapena ntchito; (pemphero ndi limodzi mwa **mwayi** wa a Khristu. Tikhoza kuyankhula ndi Mulungu ngati mmene timayankhulira ndi abwenzi. Tikhoza kufunsa Mulungu Atate pa zinthu zimene tikufuna. Ichi ndi chifukwa chake pemphero ndi mchitidwe wa paderadera kapena **mwayi** kwa Akhristu.)

4. **chipembedzo** *(mfotokozi*): kufotokozera china chake cha chipembedzo kapena mpingo; (timagwiritsa ntchito mawu a **chipembedzo** tikamanena za chipembedzo kapena mpingo.)

5. **khalani** (*mneni*): khalani; khalani pa malo omwewo; (mu vesi ili, **khalani** akutanthauza kuti khalani mwa Yesu Khristu. Timasankha ndi Yesu osati kumusiya.)

6. **chifuniro cha Mulungu** (*dzina la mawu*): chimene Mulungu amafuna pa anthu onse; (**chifuniro cha Mulungu** chimatchedwanso chifuniro cha Mulungu.)

**Phunziro 5**

**AKHRISTU AMAGAWANA NDI MULUNGU.**

***Vesi Loloweza:***

> "Chifukwa chake mungakhale mudya, mungakhale mumwa, mungakhale muchita kanthu kena, chitatani zonse ku ulemelero wa Mulungu" (1 Akorinto 10:31)

Kodi mungapemphere pemphero iri?

> *Mulungu, ndikhulupirira mwa inu. Ndikhulupirira kuti mwandipulumutsa. Ndidzakhala chifukwa cha inu m'mene ndidziwira bwino. Ndikufuna ndikutumikireni. Ndikufuna **kugawira** chilichonse chimene ndiri nacho ndi inu. Ndikufuna **kugawana** ndekha ndi inu. Mu m'dinz la Yesu ndapemphera. Amen.*

**Mtumwi** Paulo analemba kalata kwa a Khristu a kwa Akorinto. Anawauza kuti achite zonse ku ulemelero wa Mulungu. werenganinso vesi loloweza. Tifunse funso ili mu china chilichonse chimene timachita: Kodi **chikulemekeza** Mulungu?

1. Werengani Mateyu 22: 36 – 40.
   a. Kodi ndiyenera kukonda Mulungu?
   b. Kodi ndiyenera kukonda mzanga motani?
2. Werengani 1 Yohane 5: 2-3. Kodi ndingawonetse motani chikondi cha Mulungu? Kodi ndingawonetse motani kwa anthu ena?
3. Yohane akutiuza za kukhala kokondweretsa Mulungu.
   a. Werengani Yohane 12:24-25. Kodi mbewu ya tirigu iyenera kuchita chiyani isanapange mbewu zambiri?

| |
|---|
| Tirigu amapitiriza kukhala moyo mu mbewu zake za tsopano. Ndikhale mwa Yesu. Koma, ndiyenera kufa **ku dziko.** Ndiyenera kutembenuka **ku dziko**. Ndiyenera kumvera Mulungu kwa thunthu. Yesu amandipatsa moyo. |

b. Kodi ndi chifukwa chiyani ndiyenera kutsata ndi kumvera Yesu? (Yohane 12:25)

c. Ndisakhale **odzikonda.** Kodi Yesu ananena kuti Atate wake adzachita chiyani kwa aliyense amene amatumikira Yesu? (Yohane 12:26)

4. Werengani 2 Akorinto 5:17. Tsopano ndine mkhristu. Ndiri ndi **maganizo** a tsopano pa aliyense ndi china chilichonse. Kodi tsopano ndi mu banja la ndani?

| |
|---|
| Ndine wa Khristu. Munthu wakale wapiti. Tsopano, ndine munthu watsopano mwa Yesu. Ndiri ndi **maganizo** a tsopano pa zinthu. |

5. Werengani Luka 6:38. Tsopano ndikufuna kupereka zinthu. Kodi ndi chiyani chimene sindikufuna kudzisungira ndekha?

6. **Mtumwi** Paulo akulemba za **maganizo** athu pa zinthu. Werengani Aefeso 4:28. Tsopano werengani m'ndandanda uli m'musiwu. Sankhani zitatu zimene ziyenera kukhala **maganizo** athu a zinthu. (a, b, c, d, e, kapena f)

a. Kusabanso.

b. Kukhala wogwira ntchito wabwino.

c. Kudzisungira zonse ndekha. Kukhala **odzikonda.**

d. **Kugawana** ndi anthu osawuka kapena osowa.

e. Kuba pamene mungathe.

f. Kukhala wa ulesi. Osagwira ntchito.

| |
|---|
| Ndimaona anthu mwa njira ya tsopano. Ndiri ndi **maganizo** a tsopano pa athu ena. |

7. Kodi ndimawonetsa chiyani kwa ena **ndikakhudzika** nawo? (Aefeso 4:32)

8. Werengani 2 Akorinto 6:14. Kodi ndi ndani amene ndisayanjane naye?

Izi zitanthauza kuti ndisalolere kuti kuti zindipititse ku chimo. Ndikudziwona ndekha mwatsopano. Ndiri ndi **maganiz**o a pa ine mwini.

9. Werengani 1 Akorinto 6:19.

   a) Kodi ndi ndani amene amakhala mwa ine? Kotero, ndiyenera kusamalira thupi langa. Ndisachite china chilichonse choononga thupi langa.

   b) ndichifukwa chiyani ndiyenera kukhala mosamala?

Ndiyenera kugwiritsa ntchito **mwayi** wina uli onse kuti ndichite bwino. (Aefeso 5:15-16)

10. Werengani 1 Yohane 2:10. Ndi ndani amene ndiyenera kumukonda?

Izi zitanthauza kuti ndiyenera kukonda anthu onse. “M’bale wanga” amaphatikiza munthu aliyense pa dziko.

11. Mulungu analenga onse. Tsopano, werengani 1 Yohane 2:15-16. Kodi sindiyenera kukonda chiyani?

Sindikuyenera kukonda zinthu **za dziko.** Ndiyenera kutalikirana ndi **dziko.** Ndiyenera kukonda Mulungu kuposa china chiri chonse.

12. Werengani 1 Akorinto 6:20. Kodi ndi chifukwa chiyani Mulungu amafuna kuti **tizimulemekeza** ndi kumupatsa ulemu?

“Tinagulidwa ndi mtengo wapatali”. “Kugulidwa ndi mtengo wapatali” kutanthauza kuti Yesu anafa kuti atipulumutse ku machimo. “Mtengo kapena malipiro ake” ndi imfa ya Yesu.

13. Werengani Mateyu 6:33

   a) Kodi ndi chiyani chimene tiyenera kuona kapena kufuna pa zonse?

   b) China ndi chiyani chimene tiyenera kuyang’ana kapena kufuna?

Mulungu adzasamalira zosowa zathu.

14. Werengani Marko 10: 29-30. A khristu ayenera kutsatira Yesu. Kodi adzalandira chiyani mu dziko lotsatira?

15. Kodi mungafotokonzere mu chiganizo chimodzi m'mene **mudzagawirane** moyo wanu ndi Mulungu

Tsopano tikudziwa bwino m'mene **tingagawirane** miyoyo yathu ndi Mulungu. Tikhoza **kugawana** miyoyo yathu ndi anthu ena. Tikhale okoma mtima ndi a **chifundo** kwa ena. Izi **zidzalemekeza** Mulungu. tiyenera kugwiritsa ntchito **mwayi** wina uli wonse umene ungapezeke **kugawira** Yesu. Chotsatira, tiphunzira **tingagawirane** Yesu ndi ena.

*MNDANDANDA WA MAWU*

1. **Mtumwi** (*dzina la mwini mwini*): mtsogoleri mu mpingo woyambilira; ophunzira wapaderadera wa Yesu kapena otsatira Yesu

2. **ganizo** (*dzina*): fundo, ganizo kapena mamvedwe a china chake;**(Maganizo** amalamulira zimene timachita.)

3. **chifundo** *(mfotokozi)*: kukonda anthu ena ndi kusamalira sosowa zawo. (Mwachitsanzo, ali ndi **chifundo)**

4. **kulemekeza** *(mneni)*: kupereka ulemu, kutamanda, kapena kupereka ulemu kwa wina wake.

5. **mwayi** *(dzina):* mpata wochita china chake.

6. **chilungamo** *(dzina)* kukhala wosadetsedwa ndi uchimo; kukhala woyera; wolungama, komanso wangwiro pamsao pa Mulungu.

7. **kudzikonda** *(mfotokozi*): kukhala kokondweretsa ine ndekha; kusaganizira za ena ndi kuganizira za ine ndekha

8. **gawira** *(mneni)*: kupereka zimene ndiri nazo kwa ena ndi kwa Mulungu.

9. **Dziko** (*liu la m'mbuyo la dzina*): chili chonse kapena wina aliyense amene amandilepheretsa kutsata Yesu Khristu; (mu **Dziko** mumakhala makhalidwe woipa amene amawononga matupi athu. Limakhala ndi **maganizo** woipa

amene amatipangitsa kuchita zinthu molakwikwa. **Dziko** limakhala ndi zinthu zimene zimatithandiza kuiwala.)

**Phunziro 6**

## A KHRISTU AMAYANKHULIRA MULUNGU

***Vesi Loloweza:***

> "Yesu anati, 'Tiyeni pa mbuyo panga, ndidzakusandutsani asodzi a anthu'" (Mateyu 4:19)

Munthu anali ndi bwenzi lake limene limadwala. Kenaka, munthu anawona bwenzi lake. Bwenzi lake linali bwino. "Ndinapeza dokotala amene anandichiza," bwenzi linatero. "Dzina lake ndi ndani?" bwenzi linayankha. Munthu anachoka ndi chisoni. Nayenso amafuna kuti apite kwa dokotala wamphamvuyu.

Iyi ndi nkhani chabe. Koma nkhani iyi ikutikumbutsa za a Khristu. Nthawi zina, a Khristu sawuza ena za Yesu Khristu. Yesu akhoza kuthanziza anthu onse. Akhoza kuwachiritsa ku machimo awo. A khristu ayenera kuwuza anthu ena za Yesu. Mboni imanena zimene Yesu waichitira.

1. Werengani Luka 8:39. Yesu anachiritsa munthu amene anali ndi ziwanda. Munthu uyu inani mboni yabwino. Anayenda mzinda onse. Kodi munthu ananena chiyani za Yesu?

2. Buku la Yohane limatiphunzitsa m'mene tingachitire umboni. Werengani Yohane 3:32. Kenaka, sankhani yankho lolondola. (a, b, kapena c) kuchitira umboni kumatanthauza kugawira:

   a) zimene mwaphunzira kuchokera mmabuku.

   b) zimene wina wake amakuuzani.

   c) zimene mumaona ndi kudzivera.

3. Werengani Yohane 1: 40-41

   a) Andreya anapeza m'bale wake. Kodi dzina la m'bale linali ndani?

   b) Andreya anati kwa Petro, "Tapeza **Messiah.**" Kodi ndi ndani amene anatenga m'bale wake wa Yesu?

Andreya anali mboni. Anali msodzi wa anthu.

4. Werengani Yohane 6:28-29. Kodi mumakhulupirira mwa Yesu, **Messiah**? (inde kapena ayi)

Izi ndi zimene Mulungu amafuna kuti tizichita. Iyi ndi ntchito ya Mulungu. (Yohane 6:28-29)

5. Werengani Yohane 15:16

a) Kodi Mulungu amafuna kuti a Khristu aziwonetsa chiyani kapena kabala chiyani?

b) Kodi **timabala zipatso** liti?

Ndife asodzi a anthu pamene tibereka zipatso.

6. Mukhoza kukhala msodzi wa anthu ndi kubala zipatso.

a) Kodi ndi chiyani chachikulu chimene chachitika kwa inu?

b) Kodi mungalembe yankho lanu mu chiganizo chimodzi?

c) Kodi mwauza wina wake za ichi? (inde kapena ayi)

d) Kodi a Khristu angakhale okoma mtima motani kwa ena?

Iyi ndi njira imodzi imene a khristu **angabalire zipatso.**

7. Werengani Mateyu 28:18-19. Kodi Yesu amatiuza kuti tipange ophunzira a ndani?

Kenaka, tiyenera **kuwabatiza**. **Ubatizo** ndi njira imodzi ya kuchitira. **Ubatizo** umawonetsa anthu ena kuti ndife a Khristu.

8. Werengani Werengani Machitidwe 8:12 ndi 8:35-38.

a) Kodi a Khristu oyambilira anabatizika liti)

Izi ziwonetsa kuti anakhulupirira Yesu, **Mesiya**

b) Kodi munabatizika? (inde kapena ayi)

c) Ngati ayi, kodi mukuganizizira? (inde kapena ayi)

9. Werengani vesi loloweza. (Mateyu 4:19) Kodi Yesu anati adzatipanga chiyani?

10. Ndiyenera kukhala okonzeka kuchitira umboni (1 Petro 3:15) Kodi ndiyenera kukhala okonzeka kupereka chiyani nthawi zonse?

| |
|---|
| Ndiyenera kukhala okonzeka kuyankha mafunso a chikhulupiriro changa. Ndiyenera kukhala okonzeka kuchitira umboni za Mulungu. |

11. Werengani Machitidwe 17:16 -17 ndi 20:20. Kodi ndi mtumwi uti amene anakumana ndi anthu mu sunagoge komanso malo a msika?

| |
|---|
| Lero, inunso muyenera kukhala okonzeka kuchitira umboni pa malo ena ali onse. |

12. Werengani Yohane 14:6.

a) Kodi ndi chifukwa chiyani tiyenera kuchitira umboni za Yesu?

b) Kodi Yesu amati ndi ndani?

| |
|---|
| Palibe munthu angabwere kwa Mulungu kupatula kudzera mwa Yesu. Yesu ndi njira yokhayo imene tingakhalire ndi moyo wosatha. |

13. Ndikhoza kuchitira umboni za Yesu. Kodi ndimuuze chiyani wina wake amene samudziwa? Kodi ndi yankho liti m'musimu? (a, b, c, d kapena e)

a. Mphoto ya chimo ndi imfa. Koma mphatso ya ulere ya Mulungu ndi moyo wosatha. Aroma 6:23)

b. Anthu onse anachimwa. (Aroma 3:23)

c. Yesaya 53:6 amati: “Tonse tasokera ngati nkhosa, tonse tayenda yense mu njira ya mwini yekha; ndipo Yehova waika pa iye mphulupulu ya ife tonse.” Izi zitanthauza kuti Yesu anafa m'malo mwathu chifukwa cha machimo athu.

d. Onse amene amakhulupirira Yesu, **Mesiya,** ndi ana a Mulungu. (Yohane1:12)

e. Tiyenera zonse izi. (zonse a,b,c ndi d zikufunika zikufunika)

14. Werengani machitidwe 14:21 -22.

a. Kodi tingawathandize motani a Khristu a tsopano?

b. Kodi tingawathandize kukhala a Khristu olimba? (inde kapena ayi)

c. Kodi **tingawalimbikitse** kukhalabe owona mu chikhulupiriro chawo? (inde kapena ayi)

15. muli ndi umboni. Akhristu ayenera akhale ndi zinthu zitatu mu **umboni** wawo:

- Chimene ndinali ndisanakhale mkhristu.
- M'mene ndinakhalira mkhristu.
- Chimene Yesu amatanthauza kwa ine
- M'mene Yesu aliri bwenzi langa.

a. Kodi mungalembe **umboni** wa ufupi umene mungauze mzanu?

b. Kodi mumadziwa anthu ena amene si ali a Khristu? (inde kapena ayi)

c. Kodi mungalembe maina atatu mwa iwo?

| |
|---|
| Akhoza kukhala abale kapena abwenzi. Akhoza kukhala anzanu okhala nawo kapena anthu a ku ntchito. |

d. Kodi muwapemphelera anthu awa? (inde kapena ayi)

e. Kodi muchitira umboni kwa iwo? Perekani **umboni** wanu kwa iwo. **Alimbikitseni**. Kukhala bwenzi kwa iwo? (inde kapena ayi)

Mwaphunzira kuti a Khristu onse ayenera kuchitira umboni. Koma mukhoza kuchita mantha kukhala **mboni.** Kodi ndi ndani amene adzakupatsani mphamvu zoyankhura? Phunziro lotsatira tiyankha mafunso amenewa kwa inu.

*MNDANDANDA WA MAWU*

1. **ubatizo** *(dzina)*: mchitidwe wapadera kapena mwambo wogwritsa ntchito madzi kwa a khristu a tsopano; (**Ubatizo** umawonetsa kuti munthu amakhulupirira mwa Yesu ngati mpulumutsi. Mu **ubatizo** anthu akhoza kusankha kumizidwa m'madzi. Kapena madzi kuikidwa pa iwo kapenanso kuwazidwa pa iwo)

2. **batiza** (*mneni)*: kugwritsa ntchito madzi ndi a khristu a tsopano mu mchitidwe wa paderadera kapena mwambo; (onani **ubatizo**)

3. **berekani zipatso** *(mneni wa dzina wa liwu losaima palokha*): kuthandiza anthu ena kudziwa za Yesu ndi kulandira Yesu ngati mpulumutsi; kupanga kapena kubereka okhulupirira mwa Yesu.

4. **limbikitsa** (*mneni*): kugwiritsa ntchito mawu kapena zochita pa wina wake kuti amve bwino mu mzimu; kupereka chiyembekezo; kuthandiza ndi kutsogolera wina wake.

5. **asodzi a anthu.**(*dzina la liwu losaima palokha*): a Khristu amene amachitira umboni za Yesu Khristu; anthu amene amathandiza enakuti adziwe

6. **sodza anthu (***mneni wa liwu losaima palokha*) **kuchitira umboni** za Yesu Khristu; kuthandiza ena kuti adziwe Yesu.

7. **Messiah** *(dzina la mwinimwini):* Yesu Khristu; wotumizidwa ndi Mulungu pa dziko kuti akakhale mpulumutsi.

8. **sunagoge** (*dzina*): tchalitchi kapena malo a chipembedzo a Yuda.

9. **umboni** *(dzina)*: mawu amene amanena zimene Yesu amatanthauza kwa munthu; (Nthawi, zambiri munthu amapereka **umboni mu tchalitchi.)**

10. **chitira umboni** (*mneni)*: kunena zimene Yesu Khristu wakuchitirani; chitira umboni Yesu ngati mpulumutsi

11. **mboni** (*dzina)*: Munthu amene amanena zimene Mulungu wawachitira.

**Phunziro 7**

## AKHRISTU AYENERA KUDZAZIDWA NDI MZIMU WOYERA

***Vesi Loloweza:***

"Mudzale naye **Mzimu**" Aefeso 5:18

Mkhristu akhoza kunena kuti: "Ndikufuna kuchita zambiri za Mulungu. Koma ndine ofoka. Ndikufuna mphamvu zambiri. Ndikatero, ndikhoza kuchita zambiri za Mulungu."  pali yankho limodzi lokha pachosowa ichi. A khristu ayenera kudzazidwa ndi **Mzimu Woyera.** Mtumwi Paulo anati "Mudzale naye **Mzimu**." (Aefeso 5:18)

1. Yesu anaphunzitsa ophunzira ake. Anawauza za **Mzimu Woyera.** Yohane analemba zina mwa zimene Yesu anaphunzitsa. Werengani Yohane 7:38- 39. Kodi ndi ndani amene Yesu ananena kuti mkhristu amalandira?

| |
|---|
| **Mzimu Woyera** amabwera m'moyo mwa Mkhristu. |

2. Werengani Yohane 14:26. Kodi ndi ndani amene adzatiphunzitsa?

| |
|---|
| Mzimu Woyera ndi **nkhoswe.** **Nkhoswe** ndi munthu amene amatimvetsera. Ali ngati mthandizi. Amatithandizira pa mavuto athu. **Mzimu Woyera** ndi **Nkhoswe** ya Mulungu. |

3. Werengani Yohane 15:26. **Mzimu Woyera** ndi **Mzimu** wa choonadi. Kodi izi zikutanthauza kuti sitinganame? (inde kapena ayi)

4. Kodi amayankhula za ndani?

| |
|---|
| Werengani Yohane 3:3-5. **Mzimu Woyera** amagwira ntchito m'mitima ya anthu. Amagwira ntchito ndi ife **tikabadwanso mwa tsopano.** Komanso amagwira ntchito ndi ife tikabadwaanso mwa madzi ndi Mzimu. |

5. Werengani Machitidwe 1:8. Kodi **Mzimu Woyera** anapeka mphamvu kwa ophunzira ya kuchita chiyani?

6. Werengani Machitidwe 9:17. Saul [mtumwi Paulo] analandira Yesu Khristu ngati mpulumutsi. Kenaka kodi ndi ndani amene anauza Paulo kuti "adzazidwe ndi Mzimu Woyera"?

7. Werengani 1 Akorinto 3:1 komanso 3:3. A Khristu mu mpingo wa ku Akorinto anali ndi mavuto ambiri. Mavuto amenewa anawalepheretsa kuti asadzazidwe ndi **Mzimu Woyera.** Si anali okoma mtima kwa anthu ena. Analimbana okha okha ndi mawu. Anali ndimaganizo olakwika a wina ndi mzake. Kodi izi zinawonetsa chiyani za iwo?

8. Werengani 1 Petro 1:2. **Mzimu Woyera** amagwira ntchito mwa a Khristu mwa njira ina ya padera. **Mzimu Woyera** amachotsa zimene zimatilepheretsa kukhala a ngwiro ndi woyera. Ndipo timakhala osangalatsa Mulungu. Petro akuitcha ntchito yapadera iyi "ntchito **yopatulira** ya **Mzimu."** Kodi Yesu anapanga izi kukhala zotheka motani?

9. Werengani Yohane 17:17.

   a. Kodi Yesu anapempherera chiyani kwa ophunzira ake?

| |
|---|
| Yesu anapemphera kuti Mulungu **a wayeretse** ndi choonadi. |

   b. Kodi Yesu anapempherera inu pemphero ili? Ngati anatero, lembani pemphero koma muike dzina lanu.

10. Machitidwe 15:8-9. Liwu lakuti **kyeretsedwa** litanthauza kupaturidwa ku uchimo. Mulungu anapereka **Mzimu Woyera** kwa a khristu woyambilira. Kodi **Mzimu Woyera** anayeretsa mitima yawo ndi chiyani?

11. Werengani 1 Atesalonika 5:23. ili ndi pemphero la Akhristu onse. Paulo akupemphera kuti **lidzayeretsa** a Khristu nthawi zonse. Izi zitanthauza kuti Mulungu **adzayeretsa** mwa zonse kapena **adzatiyeretsa a** khristu onse mwa thunthu. Kodi ndi ndani amene adzatiyeretsa mmitima ndi miyoyo yathu?

12. Paulo anati, "Tidzikonzere tokha kuleka chodetsa chonse cha thupi ndi cha Mzimu, ndi kutsiriza chiyero, mkuopa kwa Mulungu." Kodi ndi chiganizo chiti mmusimu chimene *si*chikugwirizana ndi vesi iri? (a, b, c, kapena d)

   a. Tiyenera kusiya kuchita zinthu zimene zimaononga matupi athu.

   b. Sitingayeretsedwe m'moyo uno.

c. Tiziyesetsa kukhala ngati Yesu Khristu. Tizikhala woyera m'mene tingathere.

d. Tiyenera kusiya ntchito, malingaliro ndi maganizo anu.

13. Werengani Aroma 8:2. Lamulo la Mzimu wa moyo umatipanga kukhala aufulu. Kodi tinamasulidwa ku chiyani?

14. Werengani 1 Akorinto 13:13. A khristu ayenera kuwonetsa chikhulupiriro, chiyembekezo, komanso chikondi. Kodi chachikulu ndi chiyani mwa zitatuzi.

15. Aroma 5:5. Kodi chikondi cha Mulungu chimabwera bwanji kwa ife?

16. Werengani Aroma 8:4 A khristu **oyeretsedwa** amadzazidwa ndi **Mzimu Woyera.** Tsopano, safunanso kuyenda mu chikhalidwe cha uchimo. Motero, kodi amafuna kuti ayende motani.

Tsopano, **khalidwe la uchimo** sililamuliranso m'mene amakhalira. Mitima yawo **inayeretsedwa.** **Mzimu Woyera** amawapatsa njira yatsopano ya m'mene angakhalire. Amawapatsa mphamvu yomverera Mulungu.

**Mzimu Woyera** amagwira ntchito mwa a Khristu mu njira zosiyanasiyana. Amachotsa **chikhalidwe cha uchimo.** Amawapatsa mphamvu yokhala moyo wa chiyero. Amawathandiza kuti achitire umboni za Mulungu. koma poyamba, a khristu ayenera kuchita china chake. Ayenera kufunsa **Mzimu Woyera** kuti adzaze miyoyo yawo. Iwo ayenera kuzipereka kwa Mulungu mwathunthu.

17. Inu ndi Mzimu Woyera.

a) Kodi mwafunsa chidzalo cha Mzimu Woyera? (inde kapena ayi)

b) Kodi MzimuWoyera wabwera kudzadza moyo wanu? (inde kapena ayi)

c) Ngati ndi ayi, kodi mukuganizira za ichi? (inde kapena ayi)

18. Kodi mungafune kuti **Mzimu Woyera** adzaze moyo wanu? Ngati ndi choncho, apa pali zinthu zinayi zimene muyenera kuchita.

- Mufunseni Mulungu akudzazeni ndi **Mzimu Woyera.** (Luka 11:13)

- Perekani moyo wanu onse kwa Mulungu. (Aroma 12:1-2)
- Muwuzeni Mulungu kuti mukufuna kukhala woyera ndi wangwiro mkati. (Machitidwe 15:8-9)
- Landirani **Mzimu Woyera** mwa chikhulupiriro. Khulupirirani Mulungu kuti **akuyeretsani.** Mukhulupirireni kuti achita zimene walonjeza. (1 Atesalonika 5: 23-24)

*MNDANDANDA WA MAWU*

1. **wobadwaso mwa tsopano** (*mfotokozi wa liwu losaima palokha)*: amafotokozera mkhristu kapena okhulupirira; munthu amene anapulumutsidwa ku machimo,

2. **nkhoswe** (*dzina*): munthu amavetsera kwa anthu ndi kuwathandiza mavuto awo; **Nkhonswe** *(dzina la mwinimwini)*: **Mzimu Woyera; Mzimu wa** Mulungu; (**Mzimu Woyera** ngati **Nkhoswe** amatithandiza mavuto athu. Ndi mthandizi wapaderadera kwa a Khristu onse.)

3. **Mzimu Woyera; Mzimu waMulungu; Mzimu** (*dzina la mwinimwini*): Munthu wa chitatu mu utatu wa Mulungu; **Nkhoswe**; (Mulungu m'modzi mwa atatu: Atate, Mwana ndi **Mzimu Woyera. Mzimu Woyera** amapitiriza ntchito ya Yesu mdziko. **Mzimu Woyera** amatilimbikitsa ndi kutithandiza kudziwa Mulungu.)

4. **Kuyeretsedwa** (*mneni*): kupangidwa kukhala Woyera komanso kukhala wopewa chimo; kukhala wopanda chimo mu mtima; (mitima yathu komanso miyoyo yathu **imayeretsedwa** ndi **Mzimu Woyera.)**

5. **yeretsa; kuyeretsa** (*mneni*): kupangidwa kukhala woyera; kupatulidwa chifukwa cha chipembedzo; kudzipatula ku chimo ndi kudzipereka kwa Mulungu.

6. **khalidwe la uchimo** (*dzina la liwu losaima palokha*): mbali imodzi ya mkatikati mwa munthu imene imatsogolera ku chimo ndi kusamvera Mulungu.

## Phunziro 8

## A KHRISTU ALOWA MU BANJA LA MULUNGU

***Vesi Loloweza:***

> "Tisaleka kusonkhana kwathu pamodzi, monga amachita ena, komatu tidandaulirane, ndiko koposa monga momwe muona tsiku lilikuyandika" (Ahebri 10:25).

A Khristu onse ndi mbali imodzi ya banja la Mulungu. Mulungu ndi Atate wathu kumwamba. A khristu ndi abale ndi alongo. Banjali limatchedwa **Mpingo.** Onetsetsani kuti mukuwonetsa chikondi chambiri ku banja lanu la tsopano.

1. Baibulo limanena za anthu amene amatsata Yesu Khristu. Werengani Machitidwe 11:26. Kodi anthu amene amakhulupirira Yesu ndi otani?

2. Werengani 1 Akorinto 12:27. Kodi Mpingo umatchedwa chiyani?

| |
|---|
| Ziwalo za matupi athu zimagwilira ntchito pamodzi. **Mpingo** uyenera kugwilira ntchito ngati thupi la Khristu. |

3. Werengani Aefeso 5:23. Kodi mutu wa **Mpingo** ndi ndani?

| |
|---|
| "Mutu" amatanthauza Mtsogoleri. |

4. Werengani Aefeso 5:25. **Mpingo** unali ofunikira kwa Yesu Khristu. Kodi ndi chifukwa chiyani Yesu anafa pa mtanda?

5. Aefeso 5:24 amati **mpingo umvere** Khristu. **Kumvera** kumatanthauza kugonjera. Kukhala mbali imodzi ya **mpingo**, kodi ndiyenera kumvera ndani?

6. Werengani 1 Akorinto 4:17. Kodi ndi kuti kumene Paulo anaphunzitsa za Khristu?

7. Buku la Yohane lili ndi choonadi china cha **mpingo.** Werengani Yohane 13:35. Anthu adzadziwa bwanji kuti muli mu **mpingo?**

8. Werengani Yohane 21:16. Kodi **m'busa** ayenera kuchitira chiyani nkhosa zake?

| |
|---|
| Nthawi zina, **m'busa**timamutchanso m'busa wa nkhosa. Izi zitanthauza kuti **m'busa** ndi mtsogoleri wa **mpingo.** |

9. Akhristu amakumbukira Yesu mwa njira ya paderadera. Werengani 1 Akorinto 11:23-26. Mavesi awa ndi a **Mgonero wa Ambuye. Mgonero wa Ambuye,** ndi wa onse amene ali a Khristu. Anakhulupirira mwa Yesu pa **chipulumutso.** Kodi ndi ziti mwa izi zimene tiyenera kukumbukira za **Mgonero wa Ambuye**? (a, b, c, kapena d)

   a) Timakumbukira ndi mazunzo a imfa ya Yesu.

   b) Timakumbukira kuti Yesu anafa chifukwa cha machimo athu onse.

   a) Timakumbukira kuti Yesu akubweranso pa dziko.

   d) Tikumbukire zonsezi (zonse a, b ndi c ziyenera kukumbukiridwa).

10. Werengani Agalatia 6:2. Kodi ndingathandize motani anthu ena mu **mpingo**?

11. Werengani 1 Akorinto 12:4 ndi 7. Ndi ndani amene amapereka mphatso za padera kwa anthu? Ndiponso, anthu onse mu **Mpingo** akhoza kulandira thandizo.

12. **Mipingo** ina ndi yolimba ndi yokonda. **Mipingo** ina ayi. Ndi uti mwa **mipingo** yotsatirayi umene mungafune kuyamba? (a kapena b)

   a) **Mpingo** wa ku Yerusalemu. (Machitidwe 4:32-33)

   b) **Mpingo** wa ku Laudokeya. (Chivumbulutso 3:14-17)

13. Werengani Machitidwe 2:42. Kodi ndi chiyani chimene a Khristu oyambilira anatenga nthawi kuphunzirapo kuchokera kwa atumwi?

| |
|---|
| Anakhalanso ndi **chiyanjano** cha wina ndi mzake. **Ananyema mkate** ndi kudya pamodzi |

14. Kodi Ahebri 10:25 amatanthauza chiyani? Kodi vesi ili likutiuza chiyani?

Tisasiye kusonkhana pamodzi. Tilimbikitsane wina ndi mzake.

15. Kodi mukuganiza kuti muyambe **mpingo**? (inde kapena ayi) Ngati ndi inde, ndi chifukwa chiyani?

16. Mwakhulupirira Mulungu pa **chipulumutso**. Tsopano muli m'banja la Mulungu. **mwayanjanitsidwa** kapena **kulumikizana** ndi banja la Yesu Khristu. Mwayanjanitsidwa ndi a Khristu onse mwa Yesu Khristu. Muyenera kuganiza zoyamba **mpingo**. **Chiyanjano** ichi ndi chofunikira kwa a khristu. **Mpingo** ukhoza kukuthandizani kuti mukule mu chikhulupiriro chanu cha tsopano. **Abusa** anu akhoza kukuthandizani pakukulanso kwanu. Kodi ndi ziti mwa izi zimene ziri zowona za inu? (a, b, kapena c)

a) Ndayamba mpingo

b) Sindinayambe mpingo

c) Ndikuganiza zoyamba mpingo.

Tsopano mwamaliza maphunziro a Baibulo awa. Mukhala bdi masiku abwino mtsogolo pamene mukuyenda ndi Mulungu! kumbukirani:

•Khulupirirani Mulungu ndikukhala mwa iye.

•Werengani mawu ake ndi kuphunzira kuchokera kwa Iye.

•Yankhulani ndi Iye mu pemphero. Ndi mwayi wanu.

•Tumikirani Mulungu. Gawanani ndi Mulungu komanso ndi ena.

•Chitirani umboni zimene Mulungu wakuchitirani mwa Yesu.

•Perekani moyo wanu wonse kwa Mulungu. Kenaka, Funsani Mzimu Woyera kuti adzadze moyo wanu.

•Yambani mpingo kapena chiyanjano cha okhulupirira.

*MNDANDANDA WA MAWU*

1. **kunyema mkate** *(mneni wa liwu losaima palokha)*: kudya chakudya; komanso amatanthauza **Mgonero wa Ambuye.**

2. **Tchalitchi** *(dzina la mwinimwini):* Okhulupirira onse mwa Yesu Khristu; a khristu onse; anthu onse amene anapulumutsidwa kuchoka ku uchimo; anthu onse amene anakhulupirira Mulungu pa **chipulumutso**.

3. **tchalitchi** *(dzina):* chimango kapena malo amene a Khristu amakumana kukapembedza; **chiyanjano** cha a khristu okhulupirira.

4. **Chiyanjano** (*dzina*): anthu kukhala abwenzi ndi kugawana wina ndi mzake; moyo mu **mpingo** umene umene a Khristu amagawana mwa Yesu Khristu.

5. **Mgonero wa Ambuye** *(dzina la mwinimwini la liwu losaima palokha)*: njira ina ya paderadera imene a Khristu amakumbukilira imfa ya Yesu; (a khristu amagawana **Mgonero wa Ambuye** nthawi zina akakumana pamodzi.)

6. **m'busa** (*dzina*): mtsogoleri wa **mpingo** kapena **chiyanjano** cha okhulupirira; (**m'busa** amatumikira Mulungu mu **mpingo.** Amalalikira mawu a Mulungu. amathandiza a khristu kuti akule mu chikhulupiriro chawo.)

7. **chipulumutso** *(dzina)*: ntchito ya Mulungu imene amapulumutsa anthu ku machimo.

8. **amavera** (*mneni*): kulondora; kugonjera kapena kudzikhuthura ku chifuniro cha munthu wina.

9. **yanjanitsa** (*dzina*) lumikizana; kukhala pamodzi ngati thupi limodzi mu **Mpingo.**

## Mawu owonjenzera

## MAYANKHO A MAFUNSO

Apa pali mayankho oganiziridwa a mafunso mu maphunziro. Mupeza mayankho. Mukhoza kuganiziranso za mayankho ena olondola.

*Phunziro 1*

1. inde
2. (a) Yesu (Christu); (b) inu (ine, wina aliyense, anthu onse, munthu wina aliyense); (c) mulandireni; (d) lowani; (e) yankho la pawekha
3. inde
4. (a) chifukwa cha machimo athu; (b) inde; (c) yankho la pawekha.
5. Khristu (Yesu)
6. kukhululuka mosakakamizidwa
   (a) choipa; (b) siya; (c) kukhululukira mosakakamizidwa (khululuka mosakumbukanso)
8. c (Ndiyenera kukhulupirira mwa Yesu Khristu kuti andipulumutse.)
9. (a) ntchito zabwino; (b) ayi
10. Atate (Mulungu, Mulungu Atate)
11. inde
12. (a) inde; (b) inde; (c) kumwamba
13. yankho la pawekha –inde kapena ayi. Mwachitsanzo: “Ndalapa machimo anga. Yesu ndi mpulumutsi wanga. Yesu anandipulumutsa.” Mayankho ena ndi otheka.

*Phunziro 2*

1. (a) inde; (b) inde; (c) Yesu (Khristu); (d) inde; (e) inde

2. Mdierekezi (Satana)

3. kuyesedwa

4. ayi

5. limbanani ndi mdierekezi (Imani motsutsana ndi mdierekezi, osavera mdierekezi, mverani Mulungu)

6. kuphwanya lamulo la Mulungu (kusachita bwino, kusavera Mulungu)

7. inde

8. (a) yankho la pawekha. Mwachitsanzo: Ndisamachimwe (kupitiriza, kuchimwabe);
(b) ayi

9. a (Mulungu adzandithandiza kupewa yesero.)

10. choncho sitidzachmwa.

11. C (vomerezani machimo kwa Yesu ndipo lapani)

12. inde

13. chikondi

14. nkhosa (a Khristu; okhulupirira)

*Phunziro 3*

1. inde

2. inde

3. mayankho onse ndi “inde”

4. (a) sungani (mverani) (b) inde; (c) mverani (lolani; khulupiririrani; mverani; chitani; (d) inde; (e) mverani (pitirizani ku, pitirizani mu); (f) inde; (g) mverani Mulungu; (h) inde

5. chikondi

6. (a) inde; (b) moyo

7. (a) lupanga; (b) Mawu (chiphunzitso)

8. (a) ananena za mu Malemba; (b) amatiuza zimene Mulungu amafuna.

9. (a) Amatiuza malamulo a Mulungu; (b) kukumbukira malamulo a Mulungu.

10. onse ndi mayankho a pawekha.

11. yankho la pawekha

12. yankho la pawekha. Mwachitsanzo; kukula ngati Mkhristu, kudziwa chifuniro cha Mulungu, kupeza thandizo tsopano (mayankho ena ndi otheka)

*Phunziro 4*

1. m'mawa (masana)

2. nthawi zonse

3. yamikani

4. (a) chimo (zolakwa; machimo); (b) ayi

5. (a) (inde; (b) gwirizanani ndi zimene Mulungu amafuna (ndi zolingana ndi chifuniro chamulo)

6. a (pemphero;) (b) inde; (c) Atate; (d) khazikikani (khalani)

7. khulupirira

8. mayankho a pawekha

9. yang'anirani ndipo pempherani

10. c (muuzeni zimene timamva m'mitima yathu.)

11. mayankho a pawekha

12. mayankho a pawekha

*Phunziro 5*

1. (a) ndi mtima wanga onse, moyo wanga onse ndi moyo wanga wonse. tima ndi maganizo (b) monga ine mwini (ine)
2. zonse zimafunika kumvera (kupitiriza, kusunga; kuchita) malamulo a Mulungu
3. (a) kufa; (b) ndimalandira moyo (weniweni, watsopano); lemekeza
4. wa Mulungu
5. chilichonse; china chilichonse
6. (a) musabenso; (b) khalani wa ntchito wabwino, (d) gawanani ndi anthu osawuka komanso osowa
7. chikondi, kukoma mtima
8. wosakhulupirira (amene sakhulupirira Yesu)
9. (a) Mzimu Woyera; (b) Tsopano ndiri ndi Mulungu.
10. abale (alongo, anthu ena)
11. dziko
12. Yesu analipira (anandigula) ndi mtengo wapatali
13. (a) ufumu wa Mulungu; (b) chilungamo chake (zimene Mulungu afuna)
14. moyo wosatha (moyo wa muyaya)
15. yankho la pawekha

*Phunziro 6*

1. zonse zimene Yesu anamuchitira
2. (c) zimene mumawona ndi kudzimvera

3. (a) Petro; (b) Andreya

4. yankho la pawekha

5. (a); chipatso (b) pamene tichitira umboni (kupereka umboni)

6. Onse ndi mayankho a pawekha

7. anthu onse kulikonse (anthu ena)

8. (a) atakhulupirira; (b) mayankho a pawekha; (yankho la pawekha)

9. asodzi a anthu

10. yankho (umboni wanga)

11. Paulo

12. (a) Chifukwa Yesu ndi njira, chowonadi ndi moyo; (b) Yesu ndi amene amatitsogolera kwa Atate

13. e (tinene zonse mwa izi)

14. (a) Yankho la pawekha; (b) inde; (c) inde

15. yankho la pawekha

16. mayankho a pawekha

*Phunziro 7*

1. Mzimu (Woyera)

2. Mzimu (Woyera) (Nkhoswe, Mthandizi, komanso Mtonthozi)

3. inde

4. Yesu Khristu

5. Mboni (chitirani umboni)

6. Ananiya

7. Anali okonda za dziko. (a dziko; ngati anthu a dziko lapansi)

8. Ndi mwanzi (imfa) wa Yesu.

9. (a) kuwapatula (kuwapereka); (yankho la pawekha)

10. chikhulupiriro (chidaliro chawo mwa Yesu)

11. Mulungu

12. b. (Sitingayeretsedwe m'moyo uno.)

13. (lamulo la) uchimo

14. chikondi

15. Mzimu Woyera

16. Mzimu (Mzimu Woyera)

17. mayankho a pawekha.

18. mayankho a pawekha

*Phunziro 8*

1. mpingo (anthu); okhulupirira (ophunzira, otsatira); A Khristu.

2. thupi (la Khristu)

3. Khristu (Yesu)

4. kukhala Mpulumutsi wathu

5. Yesu (Mulungu)

6. mipingo

7. chikondi (cha pa wina ndi mzake)

8. kusamalira za (kutsogolera)

9. d (Tikumbukire zonse mwa zitatu izi.)

10. kuthandiza kunyamula zolemetsa zawo (ndi mavuto awo)

11. Mzimu (Woyera)

12. a (Mpingo wa ku Yerusalemu ndi chisankho chabwino.)

13. chiphunzitso (chiphunzitso)

14. limbikitsanani wina ndi mzake kukumana pamodzi.

15. (Mayankho a pawekha – koma mayankho ena abwino akhoza kukhala: kupembedza Mulungu; kukhala wa mphamvu ndikakumana ndi okhulupirira ena; kuthandizidwa ndi A Khristu ena; kuphunzira zambiri za Mulungu)

16. mayankho a pawekha